Pemphero Lingakuthandizeni Kukhala pa Ubwenzi ndi Mulungu (Gawo 2)

Zoti muchitezi zachokera m'mutu 17 wa buku lakuti *Kodi Baibulo Limaphunzitsa Chiyani Kwenikweni?* lomwe likupezeka pa jw.org/ny.

ZIMENE MUYENERA KUCHITA: Ganizirani mofatsa zimene mumakhulupirira komanso chifukwa chake mumazikhulupirira, fufuzani zimene Baibulo limaphunzitsa, komanso onani mmene mungafotokozere zimene mumakhulupirira kwa anthu ena.

KODI TIYENERA KUPEMPHERA MOTANI?

1 GANIZIRANI MOFATSA ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

Kodi anthu ena anganene chiyani?

_____

_____

Kodi **inuyo** mumakhulupirira zotani?

_____

N'chifukwa chiyani mumazikhulupirira?

_____

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

2 FUFUZANI ZIMENE BAIBULO LIMAPHUNZITSA

Tiyenera kupemphera kwa Yehova Mulungu kudzera mwa Mwana wake, Yesu Khristu, pa chilichonse chimene ndi chogwirizana ndi chifuniro cha Mulungu.
(Onani mutu 17 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani,* ndime 9-12.)

Werengani Mateyu 6:9 ndi Yohane 14:6.

Kodi mavesi amenewa akusonyeza bwanji kuti tiyenera kupemphera kwa Yehova yekha komanso kudzera mwa Yesu?

Werengani 1 Yohane 5:14.

Kodi ndi zinthu monga ziti zimene 'tingapemphe mogwirizana ndi chifuniro [cha Mulungu]'? (Zokuthandizani: Werengani Mateyu 6:9-13; Akolose 4:12; Yakobo 1:5.)

Yehova safuna kuti tizichita kumupempheratu kuti nthawi inayake tikufuna kuyankhula naye, ngati mmene anthu otchuka amachitira. Tikhoza kupemphera kwa iye nthawi ina iliyonse

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

Tiyenera kupemphera mosalekeza komanso mochokera pansi pa mtima.

(Onani mutu 17 m'buku la *Baibulo Limaphunzitsa Chiyani*, ndime 13-15.)

Werengani Mateyu 26:41 ndi 1 Atesalonika 5:17.

Kodi mavesi amenewa akusonyeza bwanji kuti Yehova satiikira malire a kutalika kwa mapemphero athu, komanso kuchuluka kwa nthawi zimene tiyenera kupemphera?

Werengani 1 Mbiri 16:36 ndi 1 Akorinto 14:16.

Kodi chinthu chofunika kutchula pamapeto pa pemphero lililonse n'chiyani?

Kodi ndi zinthu ziti zimene **inuyo** mungapempherere mlungu uno?

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania

3 FOTOKOZANI ZIMENE MUMAKHULUPIRIRA

WINA AKANENA KUTI…

Palibe vuto kupemphera kwa Yesu komanso kwa oyera mtima.

MUNGANENE KUTI…

Atsogoleri ambiri achipembedzo amaphunzitsadi zimenezo. Koma ineyo ndimakhulupirira zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

_____

WINA AKANENA KUTI…

N’kulakwa kupempherera zinthu zimene munthu ukufuna.

MUNGANENE KUTI…

Anthu ena amaganizadi choncho. Koma ndimakhulupirira kuti Baibulo limanena zosiyana ndi zimenezo chifukwa…

_____

_____

Kodi ndi lemba liti limene mungamuwerengere munthuyo?

_____

Poganizira zimene munthuyo amakhulupirira, kodi mungalifotokoze bwanji lembalo?

_____

www.jw.org © 2017 Watch Tower Bible and Tract Society of Pennsylvania